-Chifukwa chakuti anthu amenewa amakana kukhulupilira mawu a Mulungu.

-Ngati mudzimvera mawu a Mulungu tsiku lililonse, mudzasangalala kwambiri.

-Ngati simudzimvera mawu a Mulungu tsiku lililonse, mudzadandawula kwambiri.

-Ndikukuyembekezerani kuti mudzimvera mawu a Mulungu tsiku lililonse.



## PHUNZIRO LA 1

-Kodi chifukwa chiyani ine ndabwera kuno?

-Kodi ine ndabwera kuno ndi cholinga chodzaba malo anu?
-Iyayi.

-Ine sindinabwere kuno ndi cholinga chodzaba malo anu.

-Kodi ine ndabwera kuno ndi cholinga chodzaba ng'ombe zanu?
-Iyayi.

-Ine sindinabwere kuno ndi cholinga chodzaba ng'ombe zanu.

-Kodi ine ndabwera kuno ndi cholinga chidzaba ana anu akazi?
-Iyayi.

-Ine sindinabwere kuno ndi cholinga chodzaba ana anu akazi.

-Kodi chifukwa chiyani ine ndabwera kuno?

-Ine ndabwera kuno ndi cholinga chimodzi.

-Ine ndabwera kuno kudzakuwuzani uthenga ufunika kwambiri pa dziko la pasi lino.

-Ine ndabwera kuno kudzakuwuzani uthenga wa Mulungu.

-Ine sindinabwere kuno kudzakuwuzani uthenga wa munthu oyera.

-Ine sindinabwere kuno kudzakuwuzani uthenga wa munthu

wakuda.

-Ine ndabwera kuno kudzakuwuzani uthenga wa Mulungu okha.

-Kodi amfumu atakuyitanani kuti akakuwuzeni uthenga ofunika kwambiri, mungabwere?
-Inde, mungabwere.

-Kodi mungabwere chikukwa chiyani?

-Mungabwere chifukwa chakuti amfumu ali ndi uthenga ofunika kwambiri.

-Kodi ndi uthenga otani umene ungakhale ofunika kwambiri kuposa wa amfumu?

-Uthega wa Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani uthenga wa Mulungu ndi ofunika kwambiri kuposa  uthenga wa munthu wina aliyense?

-Ndikufuna ndikuwuzeni kufunika kwa uthenga wa Mulungu kuposa uthenga wa munthu wina aliyense.

-Kodi ndani mwa inu amene sananameko?

-Anthu onse ananamako.

-Ngakhale ine amene, ndinanamako kalelo.

-Anthu oyera onse ananamako.
-Anthu akuda onse ananamako.
-Anthu onse ananamako.



-Pamafunika kuphunzira kukolora.

-Ngati m’mene amafunikira masiku ambiri kuti munthu aphunzire kulima, chomcho pamafunikanso masiku ambiri kuti munthu aphunzire mau a Mulungu.

-Ichi ndi chifukwa chakuti muli chowona chenicheni m’mawu a Mulungu.

-Ngati mudzimvera mawu a Mulungu masiku ambiri, mudza-phunzira zinthu zambiri zowona zenizeni za Mulungu.

-Apa pali chitsanzo china:

-Kodi mumadya chakudya tsiku lililonse?
-Inde, mumadya chakudya tsiku lililonse.

-Kodi chifukwa chiyani mumadya chakudya tsiku lililonse?
-Chifukwa chakuti thupi lanu limafuna chakudya tsiku lili-lonse.

-Mukufunika kuti mudzimvera mawu a Mulungu tsiku lili-lonse ngati m’mene limafunila chakudya thupi lanu tsiku lili-lonse.

-Kodi nanga ngati simukudya chakudya tsiku lililonse, chidzakuchitikirani chiyani?
-Mudzafa.

-Ngati simukumvera mawu a Mulungu tsiku lililonse, mudzafanso.

-Kodi chifukwa chiyani anthu ena sakuwadziwa mawu a Mulungu?
-Chifukwa chakuti anthu amenewa amakana kumvera mawu a Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani mawu a Mulungu onse ndi owona okhawokha?
-Chifukwa chakuti Mulungu sanama.

-Chifukwa chakuti Mulungu amalankhula zowona zenizeni.

-Ine ndawerenga mawu a Mulungu M'buku Lake, ndipo ndikudziwa kuti mawu a Mulungu onse ndi owona.

-Ngati mudzimvera mawu a Mulungu, mudzadziwa kuti mawu a Mulungu onse ndi owona okhawokha.

-Ichi ndi chifukwa chakuti Mulungu sanama.
-Ichi ndi chifukwa chakuti Mulungu amalankhula zowona zenizeni.

-Mulungu ali ndi zinthu zambiri zakuti atiwuze.

-Mchocho patenga masiku ambiri kuti ndikuphunzitseni mawu a Mulungu.

-Apa pali chitsanzo:

-Kodi pamafunika masiku angati kuti munthu aphunzire kulima?
-Pamafunika masiku ambiri, sichomcho?

-Kodi chifukwa chiyani pamafunika masiku ambiri kuti munthu aphunzire kulima?
-Chifukwa chakuti pali zinthu zambiri zofunika kuphunzira.

-Pamafunika kuphunzira kulima mizere.
-Pamafunika kuphunzira kudzala mbewu.

-Pamafunika kuphunzira kupalira.



-Kodi amene sananameko ndi ndani?
-Mulungu.

-Chifukwa chakuti Mulungu yekha ndi amene sananameko, Iye yekha ndi amene angatiwuze ife zowona.

-Chifukwa chakuti Mulungu yekha ndi amene sananameko, Iye yekha ndi amene angatiwuze ife zowona za Mulungu.

-Chifukwa chakuti Mulungu yekha ndi amene sananameko, uthenga wa Mulungu ndi uthenga umene uli ofunika kwambiri kuposa uthenga wina uliwonse pa dziko la pasi lino.

-Uthenga wa Mulungu ndi ofunika kwambiri kwa amuna kuposa kugwira nchito ku munda.
-Kodi chifukwa chiyani?

-Chifukwa chakuti uthenga wa Mulungu okha ndi umene angawapulumutse amuna onse ku imfa.

-Uthenga wa Mulungu ndi ofunika kwambiri kwa akazi kuposa kuphika chakudya.
-Kodi chifukwa chiyani?

-Chifukwa chakuti uthenga wa Mulungu okha ndi umene angawapulumutse akazi onse ku imfa.

-Uthenga wa Mulungu ndi ofunika kwambiri kwa ana kuposa kuseŵera.
-Kodi chifukwa chiyani?

-Chifukwa chakuti uthenga wa Mulungu okha ndi umene ungawapulumutse ana onse ku imfa.
-Kodi uthenga wa Mulungu uli kuti?

-Uthenga wa Mulungu uli M'buku la Mulungu.
-Ili ndiye Buku la Mulungu.

-Kodi uthenga wa Mulungu unafika bwanji M'buku la Mulungu?

-Mulungu anakatha kulemba yekha Buku lakeli.
-Koma Iye sanapange zimenezo.

-Mu nthaŵi yapitayo, Mulungu anasankha amuna ena, ndipo Iye anayika Mawu Ake m'maganizo a amuna amenewo.
-Kenako amuna amenewo analemba Mawu a Muluguwo mu Buku la Mulungu.

-Amuna amene anasankhidwa ndi Mulunguwo, sanalembe mawu awo.

-Amuna amene anasankhidwa ndi Mulunguwo, analemba Mawu a Mulungu okha.

-Amuna amene anasankhidwa ndi Mulunguwo, analemba mawuwo malingana ndi m'mane Mulungu anawawuzila kuti alembe.

-Mulungu anasankha amuna 40 kuti alembe Mawu Ake mu Buku Lake.

-Amuna amene anasankhidwa ndi Mulungu kuti alembe Mawu akeŵa, sanakhale mu nthaŵi yimodzi.

-Panatenga zaka 1,600 kuti amuna anse amene Mulungu anaŵasankha alembe Mawu Ake.

-Kodi amuna amenewo analemba Mawu a Mulungu mu chilankhulo chanji?



-Kodi amuna amenewo analemba Mawu a Mulungu mu chilankhulo cha Chingelezi?
-Iyayi.

-Kodi amuna amenewo analemba Mawu a Mulungu mu chilankhulo cha Chicheŵa?
-Iyayi.

-Kodi amuna amenewo analemba Mawu a Mulungu mu chilankhulo cha Chiyao?
-Iyayi.

-Amuna amenewo analemba Mawu a Mulungu mu zilankhulo zawo.

-Amuna amene Mulungu anaŵasankhawo anali Ayuda ndi Mgiliki.

-Chomcho amuna amenewo analemba mawu a Mulungu mu zilankhulo za Chiyuda ndi Chigiliki.

-Kenako anthu ena anafika mu dziko la Ayudalo, ndipo anaŵaŵelenga mawu a Mulunguwo ndi kuŵalembaso mu zilankhulo zawo.

-Mawu a Mulungu amasulilidwa mu ziyankhulo zambiri za pa dziko la pasi lino.

-Tsopanonso mawu a Mulungu amasulilidwa mu chilankhulo chanu cha Chicheŵa.

-Kodi mawu a Mulungu, ndi angati amene ali owona?
-Onse.